Mmene Mungafotokozere Zimene Mumakhulupirira pa Nkhani ya Kugonana kwa Amuna Kapena Akazi Okhaokha

Gwiritsani ntchito tsambali kuti likuthandizeni kuganizira njira zabwino zofotokozera zimene mumakhulupirira.

“Nthawi zonse mawu anu azikhala achisomo, . . . kuti mudziwe mmene mungayankhire wina aliyense.”
—Akolose 4:6.

1



MUSANAYANKHE, GANIZIRANI IZI:

Nthawi zina anthu akamanena kuti mfundo za m’Baibulo n’zachikale, **kwenikweni** amakhala akutanthauza kuti zimene Baibulo limaphunzitsa zimasiyana ndi zimene iwo amakhulupirira. Kodi mukuganiza kuti munthuyo amaona kuti mfundo **zonse** za m’Baibulo monga zoletsa kuba, chigololo komanso kupha, n’zachikale? —Aroma 13:8-10.

Kodi mukuganiza kuti n’chiyani chikumupangitsa kukhulupirira zimenezo?	Mungamufunse mafunso ngati ati kuti mudziwe zimene amakhulupirira?	Nanga mungawerenge naye malemba ati?

KONZEKERANI ZIMENE MUNGAYANKHE

“Mfundo za m’Baibulo n’zachikale.”

“Anthu ena amaterodi. Koma ineyo ndimakhulupirira zoti . . . ”

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2

“Anthu amene amagonana ndi amuna kapena akazi anzawo sangasinthe chifukwa ndi mmene anabadwira.”

MUSANAYANKHE, GANIZIRANI IZI:

Baibulo silifotokoza kuti munthu amabadwa ndi chilakolako chofuna kugonana ndi mwamuna kapena mkazi mnzake. Choncho m’malo mokambirana mmene khalidweli **limayambira**, ndi bwino kukambirana za **kuipa kwa khalidwelo**.

Tiyeni tiyerekeze. Kodi ndi makhalidwe ngati ati amene anthu ena anawazolowera? Mwachitsanzo, lemba Miyambo 29:22 limanena kuti anthu ena ‘**amakonda** kukwiya’ komanso ‘**amakonda** kupsa mtima.’ Mtumwi Paulo anafotokozapo zomwe iyenso ankachita. Ananena kuti: “Pamene ndikufuna kuchita chinthu chabwino, choipa chimakhala chili ndi ine” (Aroma 7:21) Koma kodi tiyenera kukhutiritsa chilakolako chilichonse chomwe tingakhale nacho?

Kodi mukuganiza kuti n’chiyani chikumupangitsa kukhulupirira zimenezo?	Mungamufunse mafunso ngati ati kuti mudziwe zimene amakhulupirira?	Nanga mungawerenge naye malemba ati?
_____	_____	_____
_____	_____	_____
_____	_____	_____

KONZEKERANI ZIMENE MUNGAYANKHE

“Anthu amene amagonana ndi amuna kapena akazi anzawo sangasinthe chifukwa ndi mmene anabadwira.”

“Baibulo silifotokoza ngati munthu amabadwa ndi chilakolako chofuna kugonana ndi mwamuna kapena mkazi mnzake. Koma zomwe **limanena** n’zakuti . . . ”

_____

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3

“Uyenera kusintha mmene umaonera anthu omwe amagonana ndi amuna kapena akazi anzawo.”

MUSANAYANKHE, GANIZIRANI IZI:

Kodi n’kutheka kuti munthuyo ali ndi mnzake kapena wachibale amene amagonana ndi amuna kapena akazi anzake? Kodi akuganiza kuti ngati mukutsutsa **khalidwe** la munthu winawake ndiye kuti mumadana ndi **munthuyo?** Kodi munthuyo **akumvetsadi** maganizo anu pa nkhani ya kugonana kwa amuna kapena akazi okhaokha?

Kapena: Kodi munganene kuti munthu amene amafuna kuti inuyo muzingoyendera maganizo ake ndi munthu wabwino?

Kodi mukuganiza kuti n’chiyani chikumupangitsa kukhulupirira zimenezo?	Mungamufunse mafunso ngati ati kuti mudziwe zimene amakhulupirira?	Nanga mungawerenge naye malemba ati?

KONZEKERANI ZIMENE MUNGAYANKHE

“Uyenera kusintha mmene umaonera anthu omwe amagonana ndi amuna kapena akazi anzawo.”

“Ndikumvetsa chimene chikukupangitsa kuganiza choncho. Komabe, . . . ”

Kuti mupeze njira zina zothandiza, onani buku la *Mayankho a Zimene Achinyamata Amafunsa* Buku Loyamba, Mutu 23 wakuti: “Kodi Ndingafotokoze Bwanji Zimene Baibulo Limanena pa Nkhani Yogonana Amuna Kapena Akazi Okhaokha?” Mungapeze bukuli pa webusaiti yathu ya www.jw.org/ny. Pitani pomwe alemba MABUKU > MABUKU

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania